Kalata ya No. 51

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

## KUITANIDWA TIKHALE OPHUNZIRA

Pamene Yesu ankayenda m'mbali mwa nyanja ya Galileya, anaona abale awiri Petro ndi Andreya akuponya maukonde ao m'nyanja. Yesu anawaitana kuti, "Tiyeni pambuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu." Nthawi yomweyo anasiya makoka awo namtsata Iye (Mateyu 4:18-20).

Lerolo, Yesu akuitanabe anthu kuti amutsate ndipo akhale ophunzira ake. Kukhala wophunzira ndi chinthu chachikulu kuposa kungovomereza Khristu kapena kulowa m'gulu lachipembedzo. Kumatanthauza kusintha kwa moyo. Kuli kudzipereka ku chifuniro ndi cholinga cha Khristu—kukhala moyo wonga wa Yesu, kusunga malamulo ake, ndi kukhazikitsa zisankho za moyo pa ziphunzitso zake. Wophunzira wa Khristu ayenera kusiya zake zonse monga mmene Petro ndi Andreya anasiyira maukonde ao kuti atsatire Ambuye.



Moyo wa wophunzira weniweni wa Khristu sukakamizidwa ndi chikondi cha dziko lapansi, chuma chake ndi zosangalatsa zake, koma umakakamizidwa ndi chikondi chozama cha zinthu za Mulungu. Zolinga, zokhumba, mapulani, ndi zolingira zimaumbidwa potsatira chitsanzo cha Khristu.

Yesu anapereka malangizo a tchutchutchu pa zimene munthu ayenera kuchita kuti akhale wophunzira. Pa Mateyu 16:24-25 akuti, "Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wake, nanditsate Ine." Kukhala wophunzira kumatanthauza kudzikana zinthu za dziko lapansi ndi kutsatira Yesu ndi njira yake mosasamala kanthu za mtengo wake. "Yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga (Luka 14:33).

Palibe malo kwa ophunzira wa mitima iwiri. Pamafunika kudzipereka ndi kudzikhuthula kwathunthu kwa moyo wa munthu kuti akhale wophunzira wa Khristu. Petro ndi Andreya sanatenge maukonde ao pamene ankatsatira Ambuye; anayenera kuwasiya m'mbuyo. Kodi ndinu wokonzeka kusiya njira zanu kuti mutsatire Khristu? Kodi ndinu wophunzira wa Yesu? Kodi anthu angayang'ane chipatso cha moyo wanu ndikuonamo chifaniziro cha Khristu?

> "Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wake, nanditsate Ine." Mateyu 16:24-25

Pachiyambi, Yesu anaitana amuna 12 kuti amutsate Iye ndi kukhala ophunzira ake. Kupatulapo Yudasi Iskariote, ophunzira ake 11 aja adadzipereka kwathunthu ku ntchito ya Khristu. Ntchito yawo inali kuthandiza anthu komanso kufalitsa uthenga wabwino. Anthu khumi mwa ophunzira 11 aja anazunzidwa ndi kuphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chao. Ophunzira a Khristu oyambirirawa anali olimba mtima, ayenera kutipatsa ife chitsanzo chakuti tikuyenera kuvomera kuitana kwa Ambuye ndikusiya ZONSE kukhala ophunzira a Yesu. ■


| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| Kuitanidwa tikhale ophunzira 1 | Mau a Mkonzi 2 | Simoni (Petro) 3<br>Andreya, Filipo, Yohane, Yakobo 4-5 | Bartolomeyo, Yudasi, Yakobo (mwana wa Alfeyo), Mateyu, Tomasi 7 | Simoni, Tadeyo 8 |

# Mau a Mkonzi



*Chifukwa chake ifenso, popeza tizingidwa nao mtambo waukuru wotere wa mboni….* — Ahebri 12:1

Kalata iyi ya Uthenga Wabwino wa Choonadi ili yosiyaniranako m'njira zina ndi makalata akale, chifukwa mulibe gawo lija la Kuphunzira Baibulo ndi nkhani zina. Ndafulumizidwa kugawana nanu mwachidule za moyo ndi imfa ya aliyense wa ophunzira 12 aja. Utumiki wao ndi kudzipereka kwao ngati nsembe zinakhudza kwambiri chiyambi cha mpingo, ndipo ena a iwo anathandiza kwambiri pakulemba Malembawa mouziridwa ndi Mulungu.

Miyoyo yodzikhuthula ya ophunzira amenewa imaonetserabe kwa ife tanthauzo la kukhala wophunzira ngakhale padutsa zaka 2,000. Ambiri a iwo analolera kuvutika ndi kufa m'malo mosiya chikhulupiriro chao mwa Khristu. Masiku ano, Akhristu ambiri amavutika ndi zinthu zazing'ono poyerekezera ndi mavuto amene ophunzirawa ankakumana nao. Ambuye atithandize ife kuvomera kuitana ndi kutsata chifuniro cha Mulungu moona mtima. Pakufunika kudzikhuthula ndi kudzipereka kwambiri. Anthu ambiri amagwira Khristu ndi dzanja limodzi pamene dzanja linalo amakhala atagwira za dziko lapansi. TAYANI lachiwirilo ndi kusiya zonse kuti mutsatire Yesu!

Pemphero langa ndi loti Mulungu akulimbikitseni ndikukutsutsani kuti mudzipereke kozama kwa Yesu Khristu pamene mukuwerenga za "Khumi ndi Awiriwo".

Michael W. Smith

January 2025

## Ophunzira a Yesu

Simoni (Petro)

Andreya (m'bale wake wa Petro)

Yakobo (mwana wa Zebedayo)

Yohane (m'bale wake wa Yakobo)

Filipo

Bartolomeyo (Natanayeli)

Tomasi

Mateyu (Levi)

Yakobo (mwana wa Alufeyo)

Tadeyo (Lebayo, Yudasi)

Simoni Mkanani / Zelote

Yudasi Iskariote

[Mateyu 10:2-4; Marko 3:14-19; Luka 6:13-16.]



*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

# Ophunzira khumi ndi awiri

Nkhani zotsatirazi za mbiri ya moyo wa munthu zimachokera ku nkhani zosiyanasiyana. Pambali pa Baibulo, pali zochepa zimene zinalembedwa zimene zili zoona. Tsatanetsatane wachokera m'zolembedwa zakale zotsutsana zomwe nthawi zina zimapereka chithunzi cha moyo ndi imfa za amunawa. Mbiri ya ophunzira khumi ndi awiri ndi chilimbikitso ndi chobetchera. Komabe, nkofunikira kuvomereza kuti Chipangano Chatsopano chimapereka chidziwitso chochulukira cha mbiri ya munthu wofunika koposa—Yesu Khristu, Mpulumutsi ndi Mombolo wathu. (Zithunzi zonse zili zongofanizira chabe.)

## PETRO

### THANTHWE, MTSOGOLERI WACHIKHULUPIRIRO KOMA WOPUPULUMA



Petro, yemwe poyamba ankatchedwa Simoni, anali msodzi wa ku Betsaida pa Nyanja ya Galileya. Kenako anakhala ku Kapernao limodzi ndi mkazi wake ndipo ankagwira ntchito limodzi ndi m'bale wake Andreya. Popeza Petro ankadziwika kuti anali wolimba mtima komanso wochita zinthu mopupuluma, mwamsanga anakhala mmodzi wa ophunzira apamtima a Yesu ataitanidwa kuti amutsatire Yesu. Yesu anampatsa dzina lakuti "Petro" (kutanthauza "thanthwe"), limene pambuyo pake linasonyeza mkhalidwe wauzimu wa Petro. Amatchedwanso "Kefa" (Yohane 1:42; 1 Akorinto 1:12; 3:22; 15:5; Galatiya 2:9) amene ndi mau a m'Chisiriya otanthauza thanthwe kapena mwala.

Petro anali mgulu la ophunzira a Yesu odalirika kwambiri, yemwe analipo panthawi zofunika kwambiri monga pamene Yesu anasandulika (Mateyu 17:1-8) ndi pa zowawa za Yesu m'munda wa Getsemane (Mateyu 26:36-37). Ngakhale kuti chikhulupiriro chake chinali cholimba, moyo wa Petro unali wolimba mtima komanso wofooka.

Iye anayenda pamadzi kupita kwa Yesu koma anayamba kumira pamene ankakaikira (Mateyu 14:29-30). Pa nthawi imene Yesu ankazengedwa mlandu, iye anamukana Yesu katatu chifukwa cha mantha. Iye analapa ndipo pambuyo pa kuukitsidwa, Yesu anabwezeretsa Petro, namupatsa ntchito yakuti "dyetsa nkhosa zanga" (Yohane 21:15-17).

Yesu atakwera kunka kumwamba, Petro anaonekera monga munthu wotsogolera mu mpingo woyambirira ndipo anaotsenera kuti analidi thanthwe pokhala osagwedezeka, olimba ndi osasunthika. Anatumikira makamaka pakati pa okhulupirira Achiyuda ku Yerusalemu. Anapereka ulaliki wake woyamba pa tsiku la Pentekoste pamene anthu 3,000 analapa natembenuka mtima (Machitidwe 2). Petro anachita zozizwitsa, kutsogolera mpingo wa ku Yerusalemu, ndi navomereza kuti Amitundu naonso akhoza kukhala okhulupirira (Machitidwe 10). Mbiri imanena kuti pambuyo pake anapita ku Antiokeya ndipo pomalizira pake ku Roma, kupitiriza utumiki wake mosawerengera kuti akazunzidwa.

Petro amadziwika kuti ndi amene analemba mabuku awiri a Chipangano Chatsopano, 1 Petro ndi 2 Petro, omwe amalimbikitsa okhulupirira kupirira m'masautso ndi kukhalabe okhulupirika. N'zochititsa chidwi kuti Yohane Marko analemba uthenga wabwino wa Marko, analemba atauzidwa ndi Petro yemwe anaona zinthuzo chamaso. Cha m'ma 64-68 AD, Petro anaphedwa ku Roma pansi pa Mfumu Nero. Mbiri imanena kuti iye anapachikidwa chozondoka pansi potsatira pempho lake, popeza anadziona kukhala wosayenerera kufa monga momwe Yesu anachitira. Moyo wake umapereka chitsanzo cha kusinthika kuchoka pa wophunzira wamantha kukhala mtsogoleri wolimba mtima. Amakumbukiridwa monga mzati wa chikhulupiriro komanso "thanthwe" la mpingo. ■

# ANDREYA

## WOLUMIKIZIRA, WOBWERETSA ANTHU KWA YESU



Andreya, mbale wake wa Petro, anali msodzi. Iye anabadwira ku Betsaida, mudzi wa asodzi womwe unali kumpoto kwa nyanja ya Galileya. Asanakhale wophunzira wa Yesu, Andreya anali wotsatira wa Yohane M'batizi, kumene anakumana ndi Yesu koyamba. Kutsatira umboni wa Yohane wonena za Yesu monga Mwanawankhosa wa Mulungu, Andreya anakhala mmodzi wa ophunzira oyambirira kutsatira Khristu (Yohane 1:35-40). Kuyankha kwake mwamsanga kunali kubweretsa mbale wake Petro kwa Yesu, kusonyeza khalidwe la Andreya lokonda utumiki.

Ataitanidwa ndi Yesu, Andreya anayenda naye limodzi ndipo anachita nawo zinthu zambiri zofunika pa nthawi ya utumiki wa Yesu. Iye amadziwika kaamba ka ntchito yake yodyetsa anthu 5,000, kumene anamuzindikira mnyamatayo wa mikate isanu ndi nsomba ziwiri (Yohane 6:8-9). Pambuyo pa kuuka kwa Yesu, Andreya anakhala mtsogoleri wodziwika mu mpingo woyamba, makamaka pakati pa Ayuda.

Anthu amanena kuti Andreya ankalalikira m'madera osiyanasiyana monga Yudeya, Samariya, m'madera ozungulira nyanja Yakuda, ku Grisi ndi ku Turkey wa masiku ano. Malinga ndi nkhani zina, iye anayenda mpaka ku Scythia (Ukraine/Russia) akufalitsa Uthenga Wabwino kwa Amitundu ndi kukhazikitsa mipingo ya Chikhristu.

Ambiri amakhulupirira kuti Andreya anaphedwa cha m'ma 60-70 AD ku Patras, Greece. Mkazi wa bwanamkubwa anachiritsidwa ndi kutembenuka, kukwiyitsa mwamuna wake, amene analamula kuti Andreya apachikidwe pa mtanda. Kutsatira pempho la mwini wakeyo, Andreya anapachikidwa pamtanda wooneka ngati X chifukwa ankadziona kuti ndi wosayenerera kufa mofanana ndi Yesu. Pamene adapachikidwa pamtanda, adalalikira kwa anthu kwa masiku awiri.

Mwa Andreya tikuphunziramo za kukhala mlaliki komanso kudzipereka kwake pakufalitsa uthenga wa Yesu. Moyo wake umapereka chitsanzo cha mzimu wakuphunzira ndi kufunika kowafikira anthu, ndi kupangitsa kuti anthu ambiri mu mpingo woyamba ayambe kutsatira Khristu. ■

# FILIPO

## WOFUNAFUNA CHOONADI, MLALIKI WACHINDUNJI



Filipo anali wochokera ku Betsaida, mzinda womwewo ndi Petro ndi Andreya (Yohane 1:44). Iye sayenera kusokonezedwa ndi Filipo mlaliki (Machitidwe 6:5). Filipo, yemwe amadziwika kuti anali wofuna kudziwa zinthu, anali mmodzi mwa ophunzira oyambirira amene Yesu anaitanidwa. Atakumana ndi Yesu, Filipo nthawi yomweyo anazindikira kuti maulosi anakwaniritsidwa mwa Yesu. Iye anakatenga mnzake Natanaele (yemwe ankadziwikanso kuti Bartolomeyo) kuti akakumane ndi Yesu, nanena kuti: "Tapeza iye amene Mose analemba za iye m'chilamulo, ndi aneneri" (Yoh. 1:45). Mau oyambawa akusonyeza kufunitsitsa kwa Filipo kowauza ena za chikhulupiriro chake ndi kuwabweretsa ena kwa Khristu.

Filipo amapezeka kangapo m'Mauthenga Abwino, ndipo nthawi zambiri ankafunsa mafunso osonyeza kuti ankafunitsitsa kumvetsa zimene Yesu ankaphunzitsa. Mu Yohane 6:5-7, Filipo anaonetsa kuti zinamukhudza kuti zitheka bwanji kudyetsa anthu 5,000, kusonyeza mbali yake yofuna kuti zinthu zilongosoke bwino. Kenako anapempha Yesu kuti awasonyeze Atate, zomwe zinachititsa Yesu kufotokoza za umodzi wake ndi Atate (Yohane 14:8-9).

Yesu atakwera kumwamba, Filipo anayamba kulalikira, ndipo mbiri yakale imasonyeza kuti ankalalikira m'madera monga Samariya, Syria, Frigiya (masiku ano ku Turkey), ndiponso madera a Girisi. Zimamvekanso kuti anafalitsa Uthenga Wabwino m'madera amene pambuyo pake anadzakhala malo amphamvu a mpingo wa Chikhristu woyambirira.

Pali nkhani zosiyanasiyana zokhudza kuphedwa kwa Filipo. Malinga ndi akatswiri ena a mbiri yakale, iye anaphedwa mu mzinda wa Hierapolis ku Phrygia (Turkey) kumene iye anapachikidwa chazondoka pa mtanda cha m'ma 80 AD. Nkhani zina zimasonyeza kuti ankalalikira kumpoto kwa Africa komwe anagendedwa ndi miyala kapena kupachikidwa ndi akakolo.

Chikoka cha Filipo chimadziwika mu ntchito yake monga mlalili wa uthenga wabwino komanso kudzipereka kwake pakufalitsa Uthenga Wabwino kumadera osiyanasiyana. Nkhani yake imasonyeza kusakanizika kwa moyo wa tsiku ndi tsiku komanso chikhulupiriro. ■

# YOHANE

## WOPHUNZIRA WOKONDEDWA WACHIKONDI NDI CHOONADI



Yohane, amene nthawi zambiri amatchedwa "wophunzira wokondedwa," anali mbale wake wa Yakobo, mwana wa Zebedayo. Iye anabadwira m'mudzi wa Betsaida, womwe unali m'mphepete mwa nyanja ya Galileya, ndipo kenako anakakhala ku Kapernao. Asanatsatire Yesu, Yohane ankagwira ntchito ya usodzi limodzi ndi bambo ake ndi m'bale wake. Yesu anamuitana iye ndi Yakobo kukhala ophunzira, ndipo posakhalitsa iwo anakhala mu gulu la ophunzira a Yesu odalirika kwambiri. Iwo anaona zochitika zambiri zofunika kwambiri mu utumiki wa Yesu, kuphatikizapo kusandulika kwake. Yohane amadziwika kuti anali mtumwi yekhayo amene anali pansi pa mtanda wa Yesu pa nthawi ya kupachikidwa kwake, kusonyeza kukhulupirika ndi chikondi chake pa Yesu. M'zaka zake zoyambirira, anachita zinthu mwaukali ndi mwaphuma, monga pamene analetsa munthu kutulutsa ziwanda (Marko 9:38-41), pamene ankafuna kuitanitsa moto kuchokera kumwamba (Luka 9:51-54). Komanso pamene analimbana kuti ndani akhale wamkulu (Mateyu 20:20-24). Koma atakula anakhala munthu wachikondi chachikulu ndi wodzichepetsa, ndipo Yesu anapereka chisamaliro cha amai ake kwa Yohane (Yohane 19:25-27).

Yesu ataukitsidwa ndi kukwera kumwamba, Yohane adagwira ntchito yofunika kwambiri mu mpingo woyamba, makamaka ku Yerusalemu. Anathandiza kwambiri kufalitsa Uthenga Wabwino pakati pa Ayuda ndipo pambuyo pake pakati pa Amitundu. Mbiri imanena kuti Yohane analalikira ku dera kumene lero timati ku Turkey, makamaka ku Efeso, kumene anakhala mtsogoleri wotchuka m'gulu la Chikhristu.

Yohane anamangidwa ku Efeso ndipo anaponyedwa m'golo wa mafuta owira; Mulungu anamupulumutsa modabwitsa. Kenako Aroma anamuthamangitsa kupita ku chisumbu cha Patmo kumene analandira masomphenya a Yesu Khristu ndipo analemba buku la ulosi la Chivumbulutso.

Yohane anatchulidwa ndi maina ena monga Yohane wa ku Patmo, Yohane Mlaliki, Yohane Wamkulu, ndi Yohane Mkuluwampingo. Amadziwika kuti ndi amene analemba mabuku asanu m'Chipangano Chatsopano amene ali Uthenga Wabwino wa Yohane, makalata atatu (1 Yohane, 2 Yohane, ndi 3 Yohane), ndi Buku la Chivumbulutso. Zolemba zake zimatsamira pa nkhani za chikondi, chikhulupiriro, ndi umulungu wa Khristu, zomwe zimapereka mapenyedwe apadera pa za umulungu.

Mbiri ya mpingo imanena kuti Yohane anakhala ndi moyo mpaka atakalamba, mwina anamwalira cha m'ma 100 AD ku Efeso. Akuti iye anafa imfa yachibadwa, zimene zimamusiyanitsa ndi ambiri mwa atumwi ena amene anachita kuphedwa. Pa iyeyu tikuonapo kuti anali katswiri wa zaumulungu ndi mlaliki ndipo izi zakhudza kwambiri Chikhristu, ndipo nthawi zambiri amaonedwa ngati chitsanzo cha kukhulupirika ndi kudzipereka kwa Yesu. ■

# YAKOBO

## MWANA WA BINGU, WOPHEDWA WOLIMBA MTIMA



Yakobo, mwana wa Zebedayo ndi Salome ndiponso m'bale wake wa Yohane, nthawi zambiri ankatchedwa "Yakobo Wamkulu" pofuna kumusiyanitsa ndi Yakobo mwana wa Alufeyo. Iye anali msodzi wa ku Betsaida, ku Galileya. Pamodzi ndi mbale wake Yohane, iye ankagwira ntchito ya atate ake ya usodzi Yesu asanawaitane iwo kuti amtsate Iye (Mateyu 4:21-22). Iwo anali odziwika chifukwa cha changu chao, ndipo Yesu anawatcha Yakobo ndi Yohane, "Ana a Bingu" (Marko 3:17). Posakhalitsa Yakobo anakhala mu gulu la ophunzira a Yesu odalirika kwambiri, limodzi ndi Petro komanso Yohane, ndipo analipo pa nthawi zosaiwalika za utumiki wa Yesu. Iye anali wosalekanitsidwa ndi mbale wake Yohane.

Yakobo anachita gawo lofunika kwambiri pakati pa Akhristu oyambirira, ngakhale kuti pali zochepa zolembedwa mwachindunji ponena za utumiki wake. Utumiki wa Yakobo unakhudza kwambiri kulalikira kwa Ayuda amene anali ku Yerusalemu ndi Yudeya. Ngakhale kuti ndi nthano chabe osati zochitika, Yakobo ndi amene amanenedwa kuti adatengera uthenga wabwino ku Spain. Kusaletseka kwake pazinthu ndi changu chake pa uthenga wa Yesu zinamupangitsa kukhala mboni yolimba mtima ya Uthenga Wabwino. Komabe, kudzipereka kumeneku kupangitsa kuti Mfumu Herode Agripa Woyamba, amuone ndi diso losakhala bwino chifukwa amaona kufalikira kwa mpingo woyambirira kukhala chiopsezo ku dziko. Cha m'ma 44 AD Herode analamula kuti Yakobo aphedwe ndi lupanga (Machitidwe 12:1-2). Kuphedwa kwa Yakobo kunasintha kwambiri mpingo, pamene anakhala mtumwi woyamba kutaya moyo wake chifukwa cha uthenga wabwino.

Monga mmodzi wa ophunzira apamtima a Yesu, moyo wa Yakobo unali chitsanzo cha chikhulupiriro chosagwedezeka ndi kudzipereka kwake, zomwe zinampangitsa kukhala wodziwika kwambiri pakati pa atumwi. Kulimba mtima kwake ndi kukhulupirika kwake kwa Yesu mpaka mapeto kwalimbikitsa Akhristu kwa zaka mazana ambiri, kuzindikira dipo lake ndi kudzipereka pa kutsatira Khristu. ■

# BARTOLOMEYO (NATANAELE)

## MWISRAELE WENIWENI WOPANDA CHINYENGO



Bartolomeyo anali wochokera ku Kana ku Galileya (Yohane 21:2), mwinanso pamalo omwewo pamene Yesu anachita chozizwitsa chake choyamba. Bartolomeyo nthawi zambiri amadziwika kuti Natanaele, ndipo Filipo ndi amene adamupititsa kwa Yesu. Poyamba Natanaele ankakayikira, nafunsa kuti, "Kodi mu Nazarete mungatuluke chinthu chabwino?" (Yoh. 1:46) Koma atakumana ndi Yesu ndi kuona kuti Yesu anamudziwa monga, "M'Israele ndithu, mwa iye mulibe chinyengo" (Yoh. 1:47), Natanaele anakhulupirira mwamsanga. Mphindi imeneyi pamene Natanaele anafunsa moona mtima nakhulupirira ndi imene inapangitsa kuti Bartolomeyo adzipereke mokhulupirika kwa Yesu.

Yesu atakwera kumwamba, Bartolomeyo anafalitsa Uthenga Wabwino kumadera monga India, Mesopotamiya (Iraq), Persia (Iran), Likaoniya (Turkey), Iguputo, ndi Armenia, ndipo zolembera zina zimanena kuti anapita ku Ethiopia kapena ku Arabiya. Enanso amati iye ankalalikira uthenga wabwino ku India m'chinenero cha kumeneko, pomasulira m'zolemba kapena kuyankhula zinenero za kumaloko.

Tidzamukumbukira Bartolomeyo makamaka chifukwa cha utumiki wake ku Armenia, komwe adathandizira kwambiri pa kutembenuka mtima kwa anthu ambiri, mosasamala nkomwe zakuti amakumana ndi zokhoma kuchokera kwa ansembe achikunja. Imfa yake inali yankhanza kwambiri, ndipo ambiri amakhulupirira kuti anakhukhuluzidwa ali wamoyo nadulidwa mutu ku Armenia cha m'ma 68 AD. Nkhaniyi ikusonyeza kuti anali ndi chikhulupiriro chosagwedezeka ngakhale kuti anakumana ndi chizunzo chochuluka. ■

# YUDASI ISKARIOTE

## WOPEREKA KWA ADANI



Yudasi Iskariote anali wotchuka kwambiri chifukwa chopereka Yesu Khristu kwa adani. Akatswiri ena amati Iskariote amatanthauza "munthu wa ku Kerioti," mzinda wa ku Yudeya. Izi zikanamupanga kukhala Myuda yekha m'gululo komanso wakunja. Yudasi nthawi zambiri amaonetsedwa ngati msungichuma wa gulu koma amadziwikanso kuti anali wakuba yemwe ankaba m'chikwama cha ndalama (Yohane 12:6). Ngakhale kuti anaona zodzabwitsa za Yesu, Yudasi analola kuti umbombo ndi kusokonezeka zimulamulire. Iye anavomera kupereka Yesu kwa adani ndi ndalama zasiliva makumi atatu, zomwe zinapangitsa kuti agwidwe m'munda wa Getsemane (Mateyu 26:14-16).

Yesu atamutsutsa Yudasi, iye anamva chisoni kwambiri, nakabweza ndalamazo kwa ansembe kenaka nkudzikhweza (Mateyu 27:3-5). Mapeto ake omvetsa chisoni amasonyeza zotsatira za zisankho zake. Zimene anachita Yudasi ndi chenjezo lokhudza kusakhulupirika, umbombo, ndi kulephera kwa makhalidwe abwino, zomwe zimatikumbutsa za kulimbana kwathu ndi uchimo komanso kuti ndife ofunika chiwombolo. Moyo wake umasonyeza kuti munthu angapereke nthawi yake kwa Yesu koma osapereka mtima wake. ■

# YAKOBO (MWANA WA ALUFEYO)

## WOSADZIWIKA KWAMBIRI, KOMA OPHUNZIRA WOKHULUPIRIKA



Yakobo, mwana wa Alufeyo, kawirikawiri amatchedwa "Yakobo wocheperapo" kapena "Yakobo wamng'ono" pofuna kumusiyanitsa ndi Yakobo, mbale wake wa Yohane, amene amatchedwa "Yakobo wamkulu." Zambiri sizinenedwa za iye mu Chipangano Chatsopano, koma ayenera kuti anali wochokera ku Galileya. Mbiri imanena kuti iye anali mbale wake wa Mateyu, popeza onsewa amadziwika kuti anali "ana a Alufeyo," ngakhale kuti izi siziri zotsimikizika. Nthawi zina amanenedwa molakwika kuti anali Yakobo wolungama, yemwe anali mbale kapena msuweni wake wa Yesu.

Chifukwa chakuti zonena zokhudza iyetu zilipo zochepa kwambiri mu Chipangano Chatsopano, zambiri za zokhudza Yakobo zimachokera ku mbiri ya mipingo yoyambirira. Nkhani zina zimaonetsa kuti iye analalikira ku Yudeya ndipo kenako anapita ku Iguputo, namakafalitsa Chikhristu pakati pa Ayuda ndi achikunja.

Sitidziwa bwinobwino mmene anafera Yakobo, ndipo nkhani zake zimasiyanasiyana. Koma Clement waku Alexandria ndi ena amalongosola kuti adaponyedwa miyala ndi gulu la anthu kenaka ndikumenyedwa mpaka kufa cha m'ma 62 AD. Mbiri ina imanena kuti iye anapachikidwa kapena kumenyedwa ndi chibonga chochapira zovala ku Egypt. Ngakhale kuti mbiri yeniyeni ya imfa yake siidziwika bwinobwino, iye amakumbukiridwa monga mtumwi wokhulupirika, wosadziwika kwenikweni.

Ngakhale kuti Yakobo sanalembe buku lililonse la m'Baibulo, anthu amamulemekeza kwambiri chifukwa chakuti anali wotsatira wa Yesu wosasunthika. Iye akuimirira kudzipereka kodzichepetsa ndi utumiki wachete, womwe umaphatikizapo udindo wa ophunzira ofunitsitsa kufalitsa chikhulupiriro posafuna kuti adziwike. ■

# MATEYU (LEVI)

## WOKHOMETSA MSONKHO, MLEMBI WA ZIPHUNZITSO ZA KHRISTU



Mateyu, yemwe amadziwikanso kuti Levi, anali wochokera ku Kapernao, tawuni yomwe ili m'mbali mwa nyanja ya Galileya, ndipo ankagwira ntchito ngati wokhometsa msonkho asanayambe kutsatira Yesu (Mateyu 9:9). Ayuda ambiri sankawakonda anthu okhometsa msonkho chifukwa ankawaona kuti amagwirizana ndi akuluakulu a boma la Roma ndipo nthawi zambiri amakonda kuchita ziphuphu. Komabe, Yesu anamuitana Mateyu kuti amutsate, ndipo Mateyu anavomera nthawi yomweyo, nasiya ntchito yake yopindulitsa ija. Posakhalitsa, Mateyu anakonzera Yesu phwando, naitana okhometsa msonkho anzake ndi ochimwa. Izi sizinawasangalatse Afarisi koma Mateyuyo anaonetsa kuyamikira ndi kudzipereka kwake chifukwa cha moyo wake watsopano (Marko 2:15-17).

Yesu atakwera kumwamba, Mateyu anakhala mlaliki, nafalitsa uthenga wabwino poyamba pakati pa Ayuda.

Malingana ndi mbiri ya mpingo woyambirira, Mateyu analalikira kwambiri pakati pa Ayuda, zomwe zikugwirizana ndi mitu komanso maulosi zokhudza Ayuda mu uthenga wake wabwino. Ntchito yake yakulalikira iyenera kuti inafalikiranso kumadera ena, kuphatikizapo ku Ethiopia ndiponso magawo ena a dera la Parthia (Iran) ndi Syria.

Baibulo silinanene mwatsatanetsatane za mmene anaferа Mateyu, koma mbiri ya mpingo imaonetsa kuti iye anachita kuphedwa. Nkhani yodziwika bwino imanena kuti adaphedwa ku Ethiopia pochita kubayidwa. Malo ake amene izi zinachitikira komanso mmene zinakhalira sizifotokozedwa bwinobwino, komabe zolembera zambiri zimavomereza kuti adafera chikhulupiriro chake pakati pa 60-70 AD.

Mateyu amadziwika kwambiri chifukwa cha Uthenga Wabwino umene uli ndi dzina lake, womwe unalembedwa pofuna kunena mwatsatanetsatane za moyo wa Yesu ndi ziphunzitso za Yesu, komanso mmene Yesu anakwaniritsira maulosi Achiyuda onena za Mesiya. Uthenga uwu, womwe ndi umodzi mwa mabuku oyambirira kulembedwa a Chikhristu, udakali ngati mwala wapangodya wa Chipangano Chatsopano ndipo umasonyeza kudzipereka kwa Mateyu pa kufalitsa uthenga wa Khristu. ■

# TOMASI

## WOKAIKIRA, ANASANDULIKA KUKHALA WOKHULUPIRIRA WOLIMBA MTIMA



Tomasi, yemwe amadziwikanso kuti "Tomasi wokaika," amadziwika kwambiri chifukwa cha kukaikira kwake koyamba za kuuka kwa Yesu. Tomasi ayenera kuti anali wa ku Galileya, monganso atumwi ambiri. Dzina lake la Chihebri, Tomasi, limatanthauza "mapasa," ndipo m'Chigiriki amatchedwanso "Didimo," limene liri ndi tanthauzo lomwelo. Ngakhale kuti sanafotokoze zambiri za moyo wake waubwana, Tomasi akutchulidwa m'mabuku onse anai a Uthenga Wabwino ndipo amaonekera chifukwa cha kukaikira kwake komanso malingaliro ake othandiza.

Mu Uthenga Wabwino wa Yohane, maonekedwe odziwika kwambiri a Tomasi akupezeka Yesu ataukitsidwa pamene ananena kuti sadzakhulupirira pokhapokha ataona ndi kukhudza mabala a Yesu (Yohane 20:24-29). Yesu pambuyo pake ataonekera kwa Tomasi ndi kumuuza kuti akhudze mabala Ake, Tomasi akufuula kuti, "Ambuye wanga ndi Mulungu wanga," kutsimikizira chikhulupiriro chake. Kukumana uku kukuonetsa ulendo wa Tomasi kuchoka ku kukaika kupita ku chikhulupiriro cholimba ndipo amaimira iwo omwe akulimbana ndi chikhulupiriro.

Malingana ndi mbiri, Tomasi anakhala mlaliki wolimba mtima wauthenga wabwino Yesu atakwera kumwamba. Anthu amakhulupirira kuti iye anapita chakum'mawa, nakafalitsa Uthenga Wabwino ku Parthia (Iran/ Iraq). Iye anali mmodzi wa alaliki a uthenga wabwino okangalika kwambiri pakati pa ophunzira, ndipo anapita kumaiko ambiri akutali. Kenako adafika ku India cha m'ma 52 AD. Mbiri yakale ya Chikhristu, zimene amanena Akhristu ena a ku Kerala, India, amati Thomas anayambitsa magulu achikhristu m'mphepete mwa nyanja ya Malabar. Madera amenewa amamulemekezabe iye monga wodzala chikhulupiriro chawo.

Thomas akuti anaphedwa cha m'ma 72AD pafupi ndi Mylapore, komwe tsopano ndi Chennai, India. Malinga ndi zolemba za Akhristu oyambirira, iye anaphedwa ndi mkondo pamtima, mwinamwake chifukwa chakuti akuluakulu achipembedzo akumaloko anatsutsana naye. Zimene tikuphunzirapo pa moyo wake ndi zakuti tikumuona iye poyamba ali wokaika kenaka ndi kuyamba kukhala okhulupirira makamaka mu m'magulu achikhristu ku India. ■

# SIMONI (MKANANI/M'ZELOTE)

## WOKONDA ZOUKIRA ANASANDUKA WOTSATIRA WACHANGU



Simoni Mzelote ankadziwikanso kuti Simoni wachangu kapena Simoni Mkanani. Iye akutchedwa "Mzelote," zimene zikuonetseratu kuti anali kugwirizana ndi gulu la ndale lachiyuda limene linkafuna kulanda ulamuliro wa Aroma mu Yudeya pogwiritsa ntchito njira iliyonse imene ingatheke, kuphatikizapo kuchita zaupandu. Izi zikusonyeza kuti anali wokonda kwambiri dziko lachiyuda ndipo ayenera kuti anali ndi mkwiyo waukulu.

Anthu ambiri amakhulupirira kuti Simoni amachokera ku Galileya, monganso atumwi ena ambiri. Mu ndandanda wa atumwi opezeka m'mabuku a Uthenga Wabwino, nthawi zina Simoni amatchedwa "Mkanani ," kutanthauza malo amene iye anachokera m'malo mwa fuko lake, kapena lingachokere ku liwu la Chiaramu lakuti "kwanana ," kutanthauza "wachangu."

Yesu ataukitsidwa, Simoni anakhala mlaliki wokangalika, kufalitsa uthenga wabwino m'madera osiyanasiyana. Mbiri ya mpingo oyambirira imasonyeza kuti iye ankalalikira m'madera monga Iguputo, kumpoto kwa Africa, mwina mpaka ku Britain ndi Perisiya, ngakhale kuti nkhani zimenezi n'zosiyana komanso zilibe umboni wokwanira.

Tsatanetsatane okhudza imfa ya Simoni ngosatsimikizika kwenikweni, ndipo mbiri ya zimene zinachitika pakufa kwake sizigwirizana. Mabuku ena amati iye anaphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chake cha m'ma 65-70 AD, mwina pochekedwa pakati kapena kupachikidwa ku Britain. Zonenedwa zina zimati iye anaphedwa ku Persia pamodzi ndi Tadeyo.

Simoni Mzeloti amakumbukiridwa kuti anali wodzipereka ku ziphunzitso za Yesu komanso kufalikira kwa mpingo woyamba wachikhristu. Ngakhale kuti anali mmodzi wa atumwi odziwika pang'ono, kudzipereka kwachangu kwa Simoni pa kufalitsa uthenga wa Khristu kumatikumbutsa za zikhalidwe zosiyana-siyana otsatira a Yesu ndi zimene anachita. Amaonetsanso kwa onse moyo wosinthika wodzipereka ku mtendere ndi umodzi. ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

# TADEYO (LEBAYO, YUDA)

## WOLIMBIKITSA, WOGANIZA NDI WOFUNAFUNA MOZAMA



Tadeyo, wotchedwa Yudasi (kapena Yuda), mwana wa Yakobo, nthawi zina ankatchedwanso Lebayo. Jerome, katswiri wamaphunziro wa m'zaka za mma 400AD, anamutchula iye "Wapatatu," kutanthauza, "munthu wokhala ndi maina atatu." Dzina lake limapezeka m'ndandanda wa atumwi mu mabuku a Uthenga Wabwino; koma nthawi zambiri amaphimbidwa ndi ophunzira ena, zomwe zimapangitsa kuti tikhale ndi chidziwitso chochepa chokhudza moyo wake. Tadeyo akuganiziridwa kuti anachokera ku Galileya, monganso atumwi ambiri, ngakhale kuti zambiri zokhudza moyo wake waubwana sizidziwika.

Mu Uthenga Wabwino wa Yohane, Tadeyo amadziwika kuti anafunsa Yesu funso logwira mtima pa Phwando lomaliza. Iye anafunsa kuti, "Ambuye, chachitika chiani kuti muziti mudzionetsa nokha kwa ife, koma si kwa dziko lapansi?" (Yoh. 14:22) zimene zikusonyeza kuti ankafunitsitsa kumvetsetsa utumiki ndi ntchito ya Yesu.

Yesu ataukitsidwa, Tadeyo anakhala wokangalika pachikhulupiriro chachikhristu, komanso pa kufalitsa uthenga wabwino. Mbiri ya Mpingo imanena kuti uti iye analalikira m'madera osiyanasiyana, kuphatikizapo ku Yudeya, Samariya, Syria, Persia (Iran), ndi Armenia. Iye amanenedwa kuti anatembenuza Amitundu ambiri ndiponso nthawi zina amadziwika ndi kukhazikitsidwa kwa magulu a Akhristu oyambirira m'madera amenewa.

Zambiri zokhudzana ndi imfa ya Tadeyo zimasiyana malinga ndi mbiri, koma zolembera zambiri zimasonyeza kuti anaphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chake cha m'ma 65-80 AD. Mabuku ena amasonyeza kuti anaphedwa ku Edessa (Turkey), mwina pomenyedwa ndi zibonga kapena kugendedwa ndi miyala mpaka anafa.

Akatswiri ena amakhulupirira kuti Tadeyo ndiye analemba buku la Yuda, koma anthu ambiri amakhulupiriria kuti bukuli linalembedwa ndi Yuda wina, amene anali msuweni kapena mbale wake wa Yesu. Palibe yankho lachindunji pa mtsutsano umenewu popeza ena amaganiza kuti Tadeyo anali wachibale wa Yesu. Komabe, Tadeyo akudziwika monga chizindikiro cha chikhulupiriro ndi kudzipereka posawerengera zakuti anali wosatchuka kwambiri pakati pa atumwi. ■